NYA_TTB_0946_20161114_**script**

Ahebri : 1:1-2

Mutu : Kristu ndiye woposa aneneri onse

Ndipereka moni wa Kumwamba kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tsono lero titsogozedwa ndi mau apa Chibvumbulutso 5:9, amene akuti, “Ndipo ayimba nyimbo yatsopano, ndi kunena, muyenera kulandira bukulo, ndi kumasula zizindikiro zake; chifukwa mwaphedwa, ndipo mwagulira Mulungu ndi mwazi wanu anthu a mapfuko onse, ndi manenedwe onse, ndi mitundu yonse.”

Mupologalamu yatha, tinali kukambirana za mau otsogolera buku la Ahebri, ndipo lero pa Ahebri 1:1-2, tiunika nkhani yakuti Kristu ndiye woposa aneneri onse.

Ahebri 1

Pano tiyeni tiyambe ndi mau akuti gawo ili, la kalata ino likukamba za ziphunzitso zosiyana-siyana. Pamene gawo lotsiriza la kalatayomweyi, likuonetsa moyo weni-weni umene ukuti Kristu ndiye amene amadza ndi ziphunzitso motsatiranandi ntchitozake zabwino. Ndiye pfundo yaikulu yomwe ikupezeka m’bukulindiyomwe ikuonetsa ukulu wa Yesu Kristu. Tere

ndikofunika kutsamira kwambiri pa malonjezo ya Ambuye wathu Yesu Kristu, amene adanena kuti pamene Mzimu wa Mulungu udzadza pa ife, udzationetsa zinthu za Kristu monga akulankhula pa Yohane 16:12-15, kuti, “Ndiri nazo zambirinsozakunena kwa inu, koma simungathe kuzisenza tsopano lino. Koma atadzaIyeyo, Mzimu wa choonadi, adzatsogolera inu m’choonadi chonse; pakuti sadzalankhula za Iye mwini; koma zinthu ziri zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirinkudzaadzakulalikirani. Iyeyoadzalemekeza Ine; chifukwa adzatenga za mwa Ine, nadzalalikirakwa inu. zinthu ziri zonse Atate ali nazo ndi zanga; chifukwa chake ndinati, kuti atenge za mwa Ine, nadzalalikira kwa inu.”

Tsono pamene tisanthula kalata imeneyi, tiyenera kukhala tcherupopeza ndiyo kalata yoperekedwa kwa Ahebri, amene anakhulupirira Ambuye Yesu Kristu, amene anali pakati-kati pa nyengo ziwiri. Taonani iwowa analim’nyengo momwe chilamulo chimayenera kutha.Kunena kuti nsembe zonse zomwe zinali kuperekedwa m’kachisi, zomwe zinali zopindula, koma tsopano zakhala zopanda ntchito. Kutanthauza kuti Mulungu

amafunitsitsa kuti wokhulupirira aonetchimo lake, lomwe lidzaonetsedwa poyera m'kalata imeneyi. Ndiye tikunenetsa kuti ngakhale kalata iyi, inalembedwa kufuna kuthandiza Ahebri wokhulupirira, koma muli ziphunzitso zomwe ndizothandiza wokhulupirira amitundu yonse. Pachifukwa chimenechi, tikunenetsa kuti iyi, ndi kalata yomwe ndi yofunika kwambiri kwa inu ndi ine lero lino. Komabe ndikofunikansokutsindika kunena kuti madera ambiri a kalata imeneyi, akukhudza kwambiri Ahebri wokhulupirira maka-maka pamene akunena kuti Kristu ndiye wopambana aneneri. Awa, ndiwo mau amene angakhudze Ahebri kwambiri popeza m'chipembedzo chawo chachilamulo, anali kudalira aneneri kuti awaonetse chifuniro cha Mulungu.

1. Kale Mulungu analankhula ndi makolo athu mwa aneneri m'manenedwe ambiri ndi mosiyana-siyana.

Tsono ine, ndachita chidwi kuti ndime iyi, ikuyamba ndi liwu lakuti Mulungu.Kutsimikiza kuti bukuli linakhazikika kwambiri pa dzina la Mulungu.Kutanthauza kuti pamene munthu achita zinthu zina, amayenera kukhala ndi malo ake oyambira komanso otsamira. Nkhani ikunena kuti pamene munthu wapeza umboni wokwanira

wa zinthu zomwe zikumubvuta, amatsimikiza kuti pali nkhani yomwe iyenera kupita kubwalo la oweruza.

Koma tikunena kuti m'buku la Ahebri monganso m'buku la Genesis, mulibe ganizo lofunakufufuza ndi kuonetsa kuti Mulungu alipo ayi, koma kungotsimikiza kuti alipodi.Ndikunena mau amenewa chifukwa pamene munthu aona thambo la Kumwamba, ayenera kutsimikiza kuti Mulungu alipo, ndipo ngati inu simungaone chimenechi, ndiye kuti kalipo kanthu kena kakekoipa mwa inu.Tamvani Masalmo 19:1, akunena kuti, "Zakumwamba zimalalikira ulemerero wa Mulungu; ndipo thambolionetsa ntchito ya manja ake." Kutsindika kuti ngati chilengedwe chikuonekachi, sichitanthauza china chake kwa inu, ndiye kuti muli ndi bvuto lalikuru mkaganizidwekanu. Kutsimikiza mau aja amati, "Wauchitsiruamati mumtima mwake, kulibe Mulungu (Masalmo 14:1).

Tsono pamene titsatira ndime yoyambayi, tipeza kuti muli ganizo lakuti Mulungu amalankhula, kotero kuti ndiye wanzeru zoposa, popeza ndiye atininkhaifenzeruyi. Koma ngati sitizindikira chimenechi, palidi bvuto lalikuru ndipo ndikofunika

kutcheramakutu kuti tione bvumbulutso limeneli m'buku lino. Kutanthauza kuti ndichinthu chanzeru kulingalira kuti Mulungu akhoza kupereka Uthenga wina uliwonse kwa ife. Tere, ndizoonadi kuti analankhula kale kwa inu ndi ine, kudzera m'mau ake a m'Baibulo. Ndiye pamene tiona verse loyambali, tipeza kuti mau a Mulungu amene tinalandira ndiwo wouzilidwa.

Ichi, ndichifukwa chake wolemba kalata iyi, akuyamba ndi chitsimikizo chonse kuti Mulungu m'mbuyomuwakhala akupereka mabvumbulutso, koma tsopano akupereka chifuniro chake m'njira yomwe ifunikadikuimvetsetsa. Mau awa, anali ofunika kwambiri chifukwa anali kupita kwa anthu amene anaphunzitsidwa choonadi kudzera mwa aneneri. Tsono monga cholinga cha wolemba kalata iyi, chinali chofuna kuonetsa kupambana kwa ziphunzitso za Uthenga Wabwino, ndi kutsogolera Ahebri kuti achoke pachikhulupiriro chawo pa miyambo yomwe inakhazikitsidwa monga mwa malamulo a m'Chipangano Chakale, kunali koyenera kubvomereza kuti chikhulupiriro chawo pa aneneri a Mulungu, chinali chokhazikika. Paulo akubvomerezakotheratu kuti zonse zimene Ahebri anali kukhulupirira pamtima pawo zinali zoyenera,

koma akuonetsanso kuti ziphunzitso zatsopano ndizo zofunika kwambiri kuzimvetsetsa.

Tsono wolembayu akunena kuti kale Mulungu analankhula mnthawizosiyana-siyana monga momwe anafunira. Kutanthauza kuti Mulungu sanapereke Uthenga wake wonse panthawi imodzi ayi.Taonani anali kuonetsa chifuniro chake kudzera m'njira yoonetsa zinthu zomwe zinachitika kale (Mbiri/History), ulosi, mnyimbo, miyambo ngakhalenso maloto.Kutanthauza kuti Mulungu kale pakugwiritsa ntchito njira izi, anali kupereka komanso kuonetsa chifuniro chake kwa makolo athu kudzera mwa atumiki monga Mose, Davide, Yesaya, Yeremiya, Mika, Zekariya, Malaki ndi ena ambiri. Awa, ndiwo anthu amene anali kupereka Uthenga wa Mulungu kwa anthu ake, monga momwe unaperekedwera monga mwakutsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu. Kutanthauza kuti mabvumbulutso anali kuonetsedwa kudzera mnjirazochuluka, lero Mulungu yemweyu akulankhula ndi inu ndi ine, mwa Mwana wake, amene anadza ndi mabvumbulutso onse a Mulungu ndi kupereka kwa munthu aliyense.Njira iyi, inaperekedwa chifukwa ulosi unali utasiidwakuyambira m'nthawi

ya mneneri Malaki, yomwe inalinso nthawi yotsiriza Chipangano Chakale.Tikunena kuti aneneri anali kudziwa magawo osiyana-siyana a chifuniro cha Mulungu, koma pamene chifuniro chonse chinabvumbulutsidwa mwa Mesiya chinafika, chakalechochinasiidwa. Iyi, ndi nkhani yomwe ili pa 1 Akorinto 13:12, pomwe Paulo akunena kuti, “Pakuti tsopano tipenyam’kalirole, ngati chimbuuzi; koma pomwepo maso ndi maso. Tsopano ndizindikiram’deramdera; koma pomwepo ndidzazindikiratu, monganso ndazindikiridwa.” Nkhani yonseyi ikupita pakuti mabvumbulutso a m’Chipangano Chakale, anali kuonetsedwa m’magawo magawo. Ichi, chikutsimikizikachifukwa chakuchulukakwaaneneri, amene aliyense anapatsidwa bvumbulutso lake-lake, pamene kudzera mwa Kristu, mabvumbulutso a Mulungu amakhala amphumphu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna mumvetsetse kuti kalata iyi, ikuonetsa kusiyana kwakaperekedweka Uthenga wa Mulungu, m’njira zakalezosiyana-siyana, ndi kuperekedwa kwa Uthenga Wabwino mwa munthu m’modzi, amene ndi Mwana wake. Kutsimikiza kuti njira yomwe Mulungu anapereka kuonetsa

chifuniro ndi mtima wake, m'masiku ano otsiriza, a Chipangano Chatsopano, ndiyo kudzera mwa Uthenga Wabwino wobveka bwino, wa Mwana wake Yesu Kristu. Kotero kuti sitiyenerakuyembekeza njira inanso yoposa iyi ayi, koma tiyenera kumva zambiri za Kristu kudzera mwa Mzimu wake. Tere ichi, ndichimene akunena pa Ahebri 1:3, pamene akuti, "Ameneyo, pokhala ali chinyezimiro cha ulemerero wake, ndi chizindikiro cheni-cheni cha chikhalidwe chake, nanyamula zonse ndi mau a mphamvu yake, m'mene adachitachiyeretso cha zoipa, anakhala pa dzanja lamanja la ukulu m'Mwamba."

Ichi, ndichifukwa chake kuyambira nthawi ya Malaki, panapita zaka mazana anayi (400 years), pasanafikenso mtumiki wina ndi cholinga chakuti pakudza Mwana wa Mulungu, adzakhaledipothera pa chiyembekezo cha munthu. Kutsimikiza kuti Mwana wa Mulungu ndiye chionetserocheni-cheni cha Mulungu monga akunena Mateyu 21:37, kuti, "Koma pambuyo pake anatumiza kwaiwo mwana wake, nati adzachitira mwana wanga ulemu." Uyu, ndiye adzaonetsa Umulungu wonse osati mwa magawo magawo monga anachita ndi aneneri ayi, koma mwa chidzalo chonse cha

Mzimu wa Mulungu mwa Iye. Kutsimikiza mau apa Yohane 3:34, amene akuti, “Pakuti Iye amene Mulungu anamtumaalankhula mau a Mulungu; pakuti sapatsa Mzimu ndi muyeso.” Ichi, ndichimene kalatayi ikutsimikizira a Yuda mwachikhulupiriro chawo mwa aneneri kuti Kristu ndiye anakwaniritsa ulosi wonse. Tamvani Chibvumbulutso 19:10, akunena kuti, “Ndipo ndinagwa pa mapazi akekumlambira iye. Ndipo ananena ndi ine, tapenya, usatero; ine ndine kapolo mnzako, ndi mnzawowa abale ako akukhala nawo umboni wa Yesu; lambira Mulungu: pakuti umboni wa Yesu ndiwo Mzimu wa chinenero.” Komanso Ambuye Yesu mwini pa Yohane 5:46, adanena kuti, “Pakuti mudadakhulupirira Mose, mukadakhulupirira Ine; pakuti iyeyu analembera za Ine.”

2. Koma pakutha pake pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuikawolowa nyumba wa zonse, mwa Iyensoanalenga maiko ndi am’Mwamba omwe.

Ndime ino ikuonetsa kuti Mulungu analankhula kale kwa ife momveka bwino kudzera mwa Mwana wake Yesu Kristu. Kutanthauza kuti ngati Mulungu angalankhulenso lero lino kwa inu kuchoka Kumwamba, ndiye kuti akubwereza zomwe

analankhula kale mwa Kristu. Kutsimikiza kuti mau otsiriza a Mulungu ku dziko lonse, ndiye Ambuye wathu Yesu Kristu.

Ndiye pamene akunena kuti, “Koma pakutha pake pa masiku ano analankhula ndi ife…” Liwu lakuti, ‘ife’, ndilo lofunika kwambiri chifukwa likuimira a Yuda onse. Tere apa, akunena kuti kale Mulungu analankhula kwa a Yudawo kudzera mwa aneneri a m’Chipangano Chakale. Mukumbukira kuti pa Mateyu 17:5, Mulungu mwini adatsimikiza za Kristu kuti, “Uyu, ndiye Mwana wanga wokondedwa, mwa Iyeyu ndikondwera, mverani Iye.” Apanso anali kulankhula kwa a Yuda, koma popeza Yehova anapereka mau ake otsiriza, mwa Ambuye Yesu Kristu, tikutsimikizadi kuti mau amenewa ndiwo otsirizanso kwa inu ndi ine lero lino. Kunena kuti inu ndi ine, tiyenera kumvera Ambuye Yesu yekha lero lino.

Ndiye pamene tigwira mau akuti, “analankhula ndi ife ndi Mwana…” zikutsimikiza kuti Yesu Kristu ndiye woposa atumiki onse a m’Chipangano Chakale popeza bvumbulutso lonse ndi lodzala mwa Iye. Kunena kuti Kristu ndiye akukwaniritsa zonse zimene Mulungu adanena m’Chipangano Chakale ndipo kuti

ndiyekhayo, amene akupereka mau otsiriza kwa inu ndi ine. Ichi, ndichimene Ambuye Yesu mwini adanena pa Yohane 16:15, kuti, “Zinthu ziri zonse Atate ali nazo ndi zanga; chifukwa chake ndinati kuti atenga za mwa Ine, nadzalalikira kwa inu.” Kutsimikiza kuti aneneri monga Yohane, Yakobo, Luka, Paulo ndi Petro ndi atumiki ena a m’Chipangano Chatsopano, ndiwo amene anali kulemba ndi kupereka bvumbulutso lonse lochokera kwa Mulungu.

Tsopano tiyeni tigwire mau akuti, “Mwana amene anamuikawolowa nyumba wa zonse.” Kutanthauza kuti Yesu Kristu ndiye amene ali ndi ulamuliro pazinthu zonse za Mulungu. Ndiye mwa mau awa, mwina inu mwafunsa kale kuti, kodi zinthu zonsezi zikupatsidwakwa Iye bwanji popeza pa Yohane 1:3, pali mau akuti, “Zonse zinalengedwa ndi Iye; ndipo kopanda Iye sikunalengedwa kanthu kali konse kolengedwa.” Yankho likunena kuti Ambuye Yesu anatenga ulamuliro wa zonse popeza ndiwo anakwanitsa chilamulo chonse cha Mulungu kotheratu, pamene Adamu munthu woyamba analephera kugwiritsa ntchito bwino ulamuliro pa zolengedwa zonse chifukwa cha uchimo.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ikunena kuti, pamene Ambuye Yesu anadza m'dziko lapansi, anakhala munthu.Koma anachita zozizwa m'njira yonse; kunena kuti anaonetsa ulamuliro pathupi lamunthu, pachilengedwe monga kuletsanamondwepanyanja, kudyetsa anthu zikwi zisanu etc.Kutsimikiza kuti ndiye anabwezeretsa zomwe Adamu anataya pakuchita uchimo uja. Tsono tikunenetsa kuti anthu onse wokhulupirira Iye, nawonso ndi wolowawa nyumba ya Atate. Tamvani Paulo pa Aroma 8:16-17, akunena kuti, "Mzimu yekha achita umboni pamodzi ndi Mzimu wathu, kuti tiri ana a Mulungu; ndipo ngati ana, pomweponsoolowa nyumba; inde olowa nyumba yake a Mulungu ndi olowa anzake a Kristu; ngati ife timva zowawa pamodzi naye, kuti tikalandirenso ulemerero pamodzi ndi Iye." Kutanthauza kuti inu ndi ine, ngati anthu wokhulupirira ndife olowa anzake a Kristu. Koma Iyeyo ndiye wolamulira, kotero kuti ali ndi mphamvu kupereka ulamuliro pachinthu china kwa inu ndi ine. Ichi, ndicho cholowa chili chosabvunda, chamuyaya chomwe chinasungidwira wokhulupirira onse. Ndiye tikunenetsa kuti Kristu ndiye woposa aneneri onse a m'Chipangano Chakale, chifukwa ndiye pothera pa mau onse, komanso ndiye amene ali ndi

ulamuliro pa zinthu zonse za Mulungu. Ndipo tikunenetsa kuti palibe mneneri ndi m'modzi yense, amene analonjezedwa kukhala wolowa nyumba ya Atate. Ichi, ndichimene wolemba kalata iyi, akuonetsa kwa a Yudawa.

Taonani pano akunena kuti, "Mwa Iyensoanalenga maiko ndi a m'mwamba momwe." Apa, sakungonena kuti Kristu anangolenga dziko kokha ayi, koma kuti ali ndi ulamuliro pachinthu china chilichonse kotero kuti amadziwa za zomwe zidzachitika m'tsogolo ndi chifukwa chake chomwe. Ichi, ndichimene Baibulolimatsimikiza kuti Mulungu ali ndi cholinga pachinthu chilichonse chomwe analenga ndiponso lero ali ndi cholinga pazinthu zonse zimene amachita.

Mwachitsanzo kuti Mulungu amayesamnjira zambiri ndi cholinga chakuti aone ngati munthu amamukondadi.Umu ndimo Adamu analephera chifukwa sanamverechonena cha Mulungu.Komanso inadza nthawi yakuyesa munthu pofuna kuona ngati munthuyuangamvere Mulungu.Iyi, ndiyo nthawi pomwe anapereka malamulo khumi.Lero, inu ndi ine, tikukhala m'nyengo yachisomo, ndipo tinapulumuka mwachisomo, kutsimikiza kuti sitikanakhoza

kukwanitsa kusunga malamulo onse ayi.Kutsimikiza kuti inu ndi ine, sitingakwanitse kufikira pamuyeso wachiyero cha Mulungu ayi. Ichi, ndichimenechichifunika kuti munthu wina aliyense achidziwe bwino kuti sitingapulumuke ndi ntchito zathu zoyera ayi, popeza sitingakwanitse kuchita ntchito zonse zoyera. Koma tiyenerezedwa pamuyeso wake mwakukhulupirira ntchito yoyenera, momwe Ambuye wathu Yesu Kristu, anakhetsa mwazi wake, kufa ndi kuuka kwa akufa.Iyi, ndintchito yokhayo, yomwe ingathe kupulumutsa inu ndi ine.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna titsirize ndi mau akuti, popeza munthu anayesedwa nalepherakusunga malamulo onse, kotero kuti kunali koyenera kuti Mulungu anapereka njira ina. Kunena kuti ife lero tikupulumutsidwa mwachisomo cha Mulungu mwini.

Ndiye tikutsindika kunena kuti Ambuye Yesu Kristu ndiye Mlengi wa dziko lonse ndipo ali ndi cholinga pa zinthu zonse achita. Mwachisoni kuti alipo anthu ena amaoneka ngati anzeru, amanena kuti dzikoli limayendalokha popanda woyendetsa. Tere ili, ndiganizo lina losonyezadi kuti munthu alibe nzeru. Taonani lero

taphunzira kuti Kristu ndiye wolenga komanso wolowa nyumba ya Atate, amene anaika cholinga pazinthu zonse.

Lero tilekeza pano. Ndipo tinali kusanthulaAhebri 1:1-2, m'mene timaunika nkhani yakuti Kristu ndiye woposa aneneri onse.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!